

Share a story today!

Nalibali  
ZIMAYAMBA NDI  
NKHANI.

# Tsiku Lapadziko Lonse Lowerenga Momveka ndi Nal'ibali

Chaka chino ndi chikondwerero chapachaka cha chi 10 cha Nal'ibali cha Tsiku Lowerenga Momveka Padziko Lonse! Tikukupemphani inu ndi banja lanu kuti muwerenge nkhani yathu yapadera, *Phwando papaki*, momveka. Inalembedwa ndi Mabel Mnensa ndipo zithunzi zinawonetsedwa ndi Rico.

Nkhani imeneyi ikupezeka m'zilankhulo zonse 11 zovomerezeka ku South Africa. Ndipo, kuti anthu ambiri asangalale ndi nkhani yathu ya Tsiku la Padziko Lonse Lowerenga m'chilankhulo chawo, nkhaniyi ikupezekanso m'**Chishona, Chifulenchi, Chichewa, Chipwitikizi, Chiswahili** ndi **Chilingala**.

Tithandizeni kuwerengera nkhani momveka kwa ana ambiri momwe tingakwanitse pa Tsiku la Padziko Lonse Lowerenga Momveka, **2 February 2022** – ndi tsiku lililonse – ndikutenga mbali mu kulimbikitsa kuwerengera ku South Africa!

## Zomwe muyenera kuchita

Lonjezani kuwerengera momveka pamodzi monga banja pa **Tsiku la Padziko Lonse Lowerenga Momveka** – komanso tsiku lililonse. Lembetsani pa [www.nalibali.org](http://www.nalibali.org) kapena tumani ku WhatsApp mawu yoti "WRAD" ku **060 044 2254**. Banja lililonse lomwe lilembetsa lidzakhala ndi mpata yolowa mu **Tsiku la Padziko Lonse Lowerenga ya wowerengera banja limodzi ndi Nal'ibali**.

Mudzalandira nkhani zowonjezera komanso malangizo ndi malingaliro za momwe mungawerengere ndi ana anu chaka chonse.



## Kulitsani chikondi chowerengera pamodzi

Mukasangalala ndi nkhani pamodzi ndi ana anu tsiku lililonse, izi:

- ★ zimawawonetsa kuti mukuganiza kuti mabuku ndi kuwerengera ndizofunikira.
- ★ zimakupatsirani zinthu zoti mukambitsirane monga banja.
- ★ zimamanga ubale wamphamvu pakati pa inu.
- ★ zimawathandiza kuona kuti kuwerengera ndi ntchito yosangalatsa komanso yopindulitsa kwambiri.
- ★ zimawaonetsa mmene timawerengera ndi mmene mabuku amagwirira ntchito.
- ★ zimawathandiza kusangalala ndi nkhani zomwe sangakwanitse kuziwerengera paokha.
- ★ zimawalimbikitsa kuti aphunzire kudziwerengera paokha ndi kuti apitirize kuwerengera.
- ★ zimathandiza kukulitsa luso lokonda kulemba ndi kukhudza maganizo kuti akwanitse kupirira bwino kusukulu ndi m'madera.

Falitsani chikondi cha nkhani!  
Tumizani nkhaniyi kapena mugawane  
ndi wina wamene mudziwa.

# Phwando ku paki

Nkhaniyi ndiyolembedwa ndi Mabel Mnensa ★ Mafanizo anachitidwa ndi Rico ★ Lomasuliridwa ndi Afrolingo

Neo, Josh ndi Hope onse anali kunyumba kwa Agogo. Iwo anali kuyankhula ndi kuseka mokweza.



“Shhhh!” Agogo anatero. “Sindikumva zomwe akunena pawailisi. Bwerani pafupi, tiyeni tonse timvere pulogalamu yomwe ndimakonda kwambiri.”

Aliyense anakhala chete ndikumvetsera. Mosayembekezereka anamva wolengeza akutchula dzina la paki yawo.

“Oo! Paki yathu ndi yotchuka!” anatero Neo.

“... ndiyeno Tiniso, yemwensu amadziwika ndi dzina lakuthi Tin, adzapanga kuchita chiwonetsero mu pakiyo masanawa pamodzi ndi gulu la woyimba la We Can Band. Oimba ochokera ku Zimbabwe, Nigeria ndi Malawi nawonso azisewera. Aliyense ndi womasuka kubwera ku phwando!” wolengezayo anatero.

“Agogo,” anatero Neo, “kodi mwamva izi? Alengeza kuti aliyense ndi womasuka kubwera. Kodi tingapite chonde? Chonde?”

Agogo anayang’ana Neo ndikumwetulira. Ngati Josh ndi Hope aloledwa kupita kumeneko, inunso mutha kupita,” anatero. Josh ndi Hope mwachangu adatumanga kukapempha chilolezo chopita kuphwando la ku paki.

Atabwelera kukatenga Neo, Hope anauza Agogo aja kuti Bella ndi amayi ake nawonso akupita.

“Chabwino, ndiye mutha kupita ngati zili choncho. Khalani pafupi wina ndi mnzake,” Agogo anatero.

Ku paki, Neo adakumana ndi Bella ndi amayi ake, ndipo Noodle analinso atabwera. “Ndikuganiza kuti aliyense wochokera m’tawuni yathu ali pano,” Neo anatero. “Ndi anthu enanso atsopano.”

“Mvetserani ...” Josh anatero. “Kodi pali ndi anthu ena amene amalankhula Chifalansa?”

“Inde!” anatero Hope. “Ndipo ndimatha kumva enanso akuyankhula Chichewa ndi Chishona.”

Neo anagwira dzanja la Hope. “Onani,” anatero, “Tin ali pa siteji! Kodi gulu la woyimba la We Can Band lili kuti?”

Hope asanayankhe, Tin adagwira maikolofoni. “Moni!” anatero. “KODI MWAKONZEKERA KUYAMBITSA PHWANDOLI?”

“Yebo, inde!” khamu la anthu linatero mokweza.

Tin anayamba kusewera gitala yake. “Bwerezani zomwe ndimayimba,” adatero akuyamba kuyimba. “Phazi lakumanzere kumbuyo.”





"Phazi lakumanzere kumbuyo," khamulo lidayamba kuyimba motero.

"Phazi lamanja kumbuyo," adayimba motero Tin.

"Phazi lakumanja kumbuyo," khamulo lidayamba kuyimbanso motero.

Josh ndi Hope anali akumwetulira komanso kuyimba limodzi ndi ena, koma Neo anali akuyang'ane poyembekezera kuwona gulu la oyimba.



"Bwerani, aliyense!" Tin anatero mokweza. "Tiyeni tisangalale! Kapena mukufuna We Can Band kuti ikuthandizeni?"

"Yebo, inde!" khamu la anthu linatero mokweza.

Tin anayang'ana-yang'ana pozungulira. "Gulu la woyimba lili kuti? Oo ayi, sindingawawone kulikonse. Si phwando ngati palibe oyimba. Ndikufuna thandizo lina. Gulu lokha ndi lomwe lingakwaniritse izi!" Tin anamwetulira akuyang'ana gulu la anthulo. "Poyamba, ndimafuna owomba ng'oma awiri."

Neo ndi Hope ndi omwe adakweza manja awo poyamba. Atakwera pa siteji, Tin adawapatsa zitini zinayi za khofi zili ndi zivindikiro za pulasitiki. Zitinizo zinali zokongoletsedwa ndi pepala lowala kwambiri komanso mabatani. Panalinso timitengo ta ng'oma toti Neo ndi Hope azigwiritsa ntchito.

"Tsopano tikufuna ogwedeza mphonda," adatero Tin.

"Josh! Sankhani Josh!" adatero Neo mokweza.

"Kodi Josh ali pano? Josh ali kuti? Tiyeni timubweretse kuno," Tin anaseka.

Josh anakweza dzanja lake. Amuna awiri adakweza wilicheya yake pa siteji.

"Takulandirani, a Josh," adatero Tin. "Yesani kugwiritsa ntchito mphondazi ziwiri."

Josh adagwedezera imodzi kenako ina. Zinamveka mosiyana.

"Ndi zabwino kwambiri, adatero Tin.

"TSOPANO, LOLANI ..."

Koma asanamalize kunena, kunamveka phokoso lalikulu. Aliyense anayang'ana uku ndi uko kuti awone chinali choyambitsa phokosolo.

Kenako Noodle anathamangira kudutsa pa sitejipo, akukoka zitini zomangirizidwa pamodzi ndi chingwe kumbuyo kwake.

"Phokoso labwino!" Tin adatero mokweza. "Ndimaganiza kuti ndawataya."

Bella anathamangira ku sitejiko. "Noodle!" adamuyitana. Noodle anathamangira komwe kunali ndi Bella, zitini zikugundana mwaphokoso kumbuyo kwake.

"Palibe vuto," anatero Tin akuseka.

"Ndikuganiza kuti Noodle akufuna kukhala membala wa We Can Band. Ndiyeno ndikuganiza kuti akufuna inunso kuti mugwire ntchito limodzi nafe," anatero akuloza Bella.

Tin anathandizira Bella kukwera pa siteji ndiponso onse pamodzi adamasula zitini zomwe zinali zinamangiridwa pathupi la Noodle. Kenako Bella ndi Noodle anapita ndi kukaima pafupi ndi Neo, Hope ndi Josh.

Tin anakonzekera kusewera gitala yake ndipo adati, "LOLANI NYIMBO ZIYAMBE!"

Pomwe Tin adaloza Neo ndi Hope, awiriwa anayamba kuwomba ng'oma zawo. Kenako Tin anayamba kuimba, "Phazi lakumanzere kumbuyo," ndi kuloza ku khamulo.

"Phazi lakumanzere kumbuyo," khamulo lidayamba kuyimba motero.

Zitatero, Tin adaloza Josh ndiyeyo adayamba kugwedeza mphonda zake mogwirizana ndi kulira kwa nyimbo.

"Phazi lamanja kumbuyo," adayimba motero Tin.

"Phazi lakumanja kumbuyo," khamulo lidayamba kuyimbanso motero.

Tin adaloza Bella. Phokoso la zitini linamveka bwino pamene Bella anagwedeza ndi kumenyanisa zitinizo pamodzi. Noodle anafuula mokondwera.

Posakhalitsa phwandolo lidafika pachimake. Pamene Tin anali kuimba nyimbo zake Neo, Josh ndi Bella anali kumenya zida zoimbira. Ndiponso Noodle adali kufuula mokondwera nthawi ndi nthawi!

Kenako oyimba enawo adayimba nyimbo za kudziko lawo. Khamu la anthulo linakuwa mokondwera ndi kuwomba m'manja. Iwo adakonda chiwonetserocho!

"Mwawona," adatero Tin poyankhula ndi mamembala a We Can Band, "kagulu kakang'ono aka kathandizira kukwaniritisa zomwe zimayembekezereka!

Tikukuthokozani inu anayi ... kuphatikiza ndi Noodle, aliyense asangalala chifukwa cha phwandoli!"



# Mabanja omwe amawerengera limodzi, apambana limodzi

## Werengani ndikufotokozerani nkhani kwa mwana ALIYENSE tsiku LILILONSE

Mungakwanitse kuwerenga nkhaniyi momveka kwa ana azaka 6 kapena akulu kuposa apo. Ana azaka zapakati pa 3 mpaka 6 adzasangalala *kumvetsera* nkhaniyi pamene mukuwauza. Nazi zitsanzo za malingaliro amomwe mungagawire nkhaniyi ndi ana ang'onoang'ono.

### Musanayambe

- ★ Idziweni bwino nkhaniyi kuti muifotokozenso m'njira yanuyanu.
- ★ Ganizirani momwe mungapangire nkhaniyi kukhala yamoyo kwambiri.
  - Pangani chithunzichi chimene chimati: "Bwerani kuphwando lathu ku paki!" Ikani chithunzichi pamene ana adzachiwona.
  - Sankhani nthawi ya tsiku kuti mufotokoze nkhaniyi pamene banja lanu lonse lili pamodzi.
  - Pezani mbali za nkhani zomwe ana angagwirizane nazo, mwachitsanzo, kuchita zochitika za nyimbo ya Tin.
  - Sankhani mawonekedwe a nkhope ndi manja omwe mukufuna kugwiritsa ntchito ponena nkhaniyi, mwachitsanzo, kuyang'ana gulu la We Can Band monga Neo adachitira.
  - Sonkhanitsani ndi/kapena pangani ng'oma zosavuta, zogwedeza ndi zolira pogwiritsa ntchito malata, kapena tsitsani ndi kusindikiza zithunzi za nkhaniyi pa [www.nalibali.org](http://www.nalibali.org) kuti mugwiritse ntchito ndikuwonetsa pamene mukufotokoza nkhaniyi.
- ★ Yesetsani kunena kapena kuwerenga nkhaniyi pa nokha mokweza mawu, kapena kuchita kuti anthu ali mu nkhani imeneyo aziwerengedwa ndi wina wake wam'banja kapena mnzake. Mwa chitsanzo, gawo la nkhaniyi limene Agogo amayankhula likhoza kuwerengedwa ndi agogo anu.

### Pa nthawi ya nkhani

- ★ Fotokozerani nkhani ndi anthu ali munkhaniyi.
- ★ Auzeni ana nkhaniyi.

### Nkhani itatha

- ★ Funsani mafunso yotseguka kuti mulimbikitse ana kuganiza ndi kukambirana za malingaliro okhudzana ndi nkhani, mwachitsanzo, "Kodi mumakonda kuchita chiyani paphwando?"
- ★ Pamodzi, chitani sitepe yovina. Itanani masitepe ngati Tin anachita.
- ★ Itani ana kuti:
  - apange zida zoimbira monga ng'oma, chida chogwedeza ndi zolitsa kuchokera kuzinthu zobwezerezedwanso monga malata, pulasitiki, zingwe kapena ubweya, zopukutira zamapepala, mikanda, mabatani ndi nsonga zamabotolo, komanso zomatira, lumo ndi utoto.
  - konzani konsati kumene amagwiritsa zida zawo ndi kuimba.
  - pangani zithunzi kuchokera munkhaniyi pogwiritsa ntchito mtanda kapena dongo.



Tumizani zithunzi ndi makanema anu ndi ana anu mukusangalala ndi nkhani ya **Tsiku Lapadziko Lonse Lowerenga Momveka** pa tsamba lathu la Facebook!



**Nal'ibali** (mu chilankhulo cha siXhosa chotanthauza "nkhani ndiyi") ndi kampeni yapadziko lonse yowerengera kuti musangalale. Masomphenya athu ndi South Africa komwe **mwana aliyense** amasangalala ndi nkhani tsiku lililonse.

**Nal'ibali** ali pano kuti akulimbikitseni ndi kukuthandizani. **Lumikizani** nafe mwanjira iliyonse mwa njira izi:

f nalibaliSA

@nalibaliSA

@nalibaliSA

info@nalibali.org

*nalibali*

CHICHEWA